

Ndondomeko Mwachidule



CIVIL SOCIETY NETWORK ON CLIMATE CHANGE (CISONECC) January, 2016

NDONDOMEKO YADZIKO YOTHANA NDIKUSINTHA KWA NYENGO

Mau Mwachidule

Dziko la Malawi ndiloopsezidwa ndikusintha kwa nyengo kmansozanyengo zopitilira muyeso. Dziko lakumana ndi ziopsezo zakusintha kwanyengo zosiyanasiyana monga mvula yambiri, kusefukira, chilala, ng'amba ndi mphepo yamkuntho ndi zina. Izi zikubweretsa zovuta ndi zotsatira zoopsa pachitukuko ndi umoyo wa anthu; Mwachitsanzo, chilala chapangitsa kuti mbeu zisachite bwino zomwe zikubweretsa njala ndi kusowa zakudya mthupi. Pachifukwa ichi, ndondomeko yothana ndi kusintha kwa nyengo yapangidwa ndi choinga chothana ndi kusintha kwanyengo kuti anthu akhale ndi umoyo okhazikika. Izi zidakwaniritsidwa popereka chidziwitso, kuchepetsa zoopseza nyengo ndi zinthu zina zosowa mbali ina kupititsa patsogolo chitukuko cha zachuma polowetsa nkhani zakusintha kwanyengo mu ma pulani a dziko, Magawo achitukuko ndi mabungwe ena.



act:onaid



1.0 Mau Oyamba

Dziko la Malawindi limodzi mwamaiko amene ali pa chiopsezo cha kusintha kwanyengo chifukwa limadalira chuma chake paulimi komanso ulimi wa mvula. Dzikoli lakumana ndi zilala, ng'amaba, mvula yambiri ndi kusefukira kwamadzi ndi zina zimene zikpangitsa kusachita bwino kwa mbeu, njala, kusowa zakuday mthupi, anthu kutaya miyoyo ndi katundu. Ziopsezosi zaneke kuti zikuchulukirachulukira kuchokera mzaka za 1970. Poganzira kuti anthu akumudzi, amene ndiochukuka, omwe ndiosauka ndipo amadalira zachilengedwe paumoyo wao, ambiri mwa anthuwa amasowa kuthekera koika chuma pantchito zochepetsa, kuthetsa ndi kupititsa patsogolo ntchito zogwirizana ndi kusintha kwanyengo. Choncho ndikofunika kuti pakhale njira zozozeka zopezera ndalama kuchokera mdziko mwathu muno ndi kunja kwa dziko kuti zithandize ntchitoyi. Poganzira kuti kusintha kwanyengo ndi vuto okhudza chitukuko, ntchito zothetsa zotsatira zake ndi kulola makampani kutsatira ngodya zokweza ntchito zakusintha kwanyengo zikhoza kuthandza kudzera ku zizindikiro zachitukuko monga kuchepetsa umphawi ndikukweza umyo wabwino.

Poti ndondomeko yothana ndi kusintha kwanyengo ikufuna kutsogolera kupanga ntchito zochepetsa mipweya yoipa yoononga mlengalenga, komanso kukhala ozolowera ndi olimba ku mavuto ndi zotsatira zakusintha kwanyengo. Kapangidwe ka ndondomekoyi kakugwirizana kwambiri ndi zofuna zadziko, ndi maiko akunja. Ndondomeko idzatsogolera ndi kulumikizitsa zofunika kukwaniritsa za nthambi ya bungwe la chitukuko ladziko lonse lapansi loona kusintha kwanyengondondomeko kukwira ndi chitukuko cha dziko la Malawi yachiwiri. Ndondomekoyi idzaunikidwa ndi kukonzedwanso pakapita zaka zisanu zilizonse pofuna kuikamo zinthu zina zatsopano.

2.0 Cholinga

Cholinga chachikulu chandondomekoyi ndi kupititsa patsogolo ntchito zochepetsa ndi kuthetsa kusintha kwanyengo pofuna kukhala ndi umoyo okhazikika.

3.0 Zolinga

Ndondomekoyi ili ndi zolinga zitatu zikuluzikulu ndipo ndi izi;

- Kuonetsetsa kuti zotsatira zakusintha kwanyengo zikuthetsedwa.
- Kuthandizira kuchepetsa ndikukhazikitsa mipweya yoipa yoononga mlengalenga.

- Kulowetsamo zinthu zokhudza jenda, HIV ndi Edzi mu ntchito yakusintha kwanyengo kudzera mu mndandanda wa mabungwe oyenera.

4.0 Ngodya Zotsogolera Ndongomekoyi

Ndongomekoyi idzatsogoleredwa ndi ngodya zisanu ndi ziwiri zimene zinaikidwa Malamulo adziko lino, Bungwe ladziko lonse lapansi lona ntchito zakusintha kwanyengo la UNFCCC. Ngodyazi ndi monga izi:

- Kuteteza mafulu a anthu,
- Kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo (Jenda),
- Chitukuko chokhalitsa,
- Chitukuko chofanana;
- Owononga chilengedwe ayenera kulipira,
- The precautionary principle, ndi
- Magulu okhudzidwa ndi anthu kutengapo mbali moyenera

5.0 Magawo Ofunika a Ndongomekoyi ndichani?

Magawo asanu ndi atatu andongomekoyi ndi njira zake zokwaniritsira ndi izi:

1- Kuchepetsa Ululu wa Kusintha kwanyengo

Izi zimatanthauza ntchito ina iliyonse imene imathandiza anthu kukhala olimba, kuchepetsa mavuto akusintha kwanyengo ndi kutengerapo mwayi pa zinthu zimene zikubwera. Cholinga cha ndongomekoyi ndi ndikuchepetsa chiopsezo kwa a Malawi ndikupititsa patsogolo kudzidalira ndi kulimba ku zotsatira zakusintha kwanyengo poonetstesanso kuti chitukuko chohazikika chikuchitika. Zolinga ndi monga kukonza njira zabwino zochepetsera kusintha kwa nyengo komanso zomwe zimaphatikiza zinthu zokhudza gawo lililonse ndikuonetsetsa kuti dziko likuchita ntchito zake potsatira kusintha kwanyengo.

Ulimi- Ndongomekoyi idzaunika kulowetsa ntchito zaulimi mu mapulani kuthana ndi kusintha kwanyengo, ntchito zake pounikira kafukufuku wa kuopsezedwa kwake, kuikamo mmene anthu okhudza zachuma ndi ndale angatengerepo mbali poteteza mabanja oopsezedwa, kafukufuku wapamwamba ndi ukadaulo pa ntchito zakusintha kwanyengo, kukhazikitsa

ulimi omwe umatsatira ndondomeko zosamalira chilengedwe ndi chitukuko chakumidzi, kukhazikitsa malonda akumidzi, kukonza njira zogwiritsa ntchito uthenga wakusintha kwanyengo ndi ulimi, kukhazikitsa ulangizi wabwino, kupewa kuonongeka kwachilengedwe, kupeza mwayi wazipangizo ofanana, kupititsa patsogolo njira zamakono ndi ukadaulo ndi kupereka chidziwitso pa ukadaulo watsopano.

Madzi – Kupititsa patsogolo njira zamakono zosungira madzi, ndondomeko zabwino zosamalira malo osunga madzi ndi kupititsa patsogolo chilengedwe, kukwaniritsa lamulo lopewa kuononga mlengalenga, kulumikizitsa ndondomeko zosiyanasiyana, ndikuchita ulimi ogwirizana ndi mmene nyengo iliri.

Zaumoyo – Kupititsa patsogolo kafukufuku wazaumoyo ndi zovuta za kusintha kwanyengo pa zaumoyo, kuika zakusintha kwanyengo mu ndondomeko yazaumoyo, kulumikizitsa katoleredwe ka mauthenga pakati pa nthambi zaumoyo ndi za kusintha kwanyengo, kupereka kuthekera mmagawo achitukuko pofuna kupititsa patsogolo kumvetsetsa kugwirizana kwa kusintha kwanyengo, chidziwitso cha kaganizidwe ka zaumoyo ndi zofunika zadziko, ndondomeko zachaudya chokwanira ndi moyo wathanzi kulumikizidwa ndi njira zochepetsera mavuto azaumoyo, kuthandizira kafukufuku osiyanasiyana ndi kuunikanso ndondomeko zamaphunziro ndi mndandanda wakaphuzitsidwe zimene zingamakambe zakusintha kwanyengo ndi zaumoyo.

Kusamutsa Anthu Pokhala – Kukonza malire ndi kagwiritsidwe ntchito ka malo, kukhazikitsa ndondomeko yakasamutsidwe ka anthu ndi malo okhalopo, kukonza ndi kugawa malo, kutaya kwa zinyalala kwabwino kwa anthu okhudzidwa, kuthandizira njira zamakono zosamalira chilengedwe popanga njera ndi kupereka mwayi osangaatsa anthu amene akupanga ntchito zothandizira kuthana ndi kusintha kwanyengo.

Mphamvu ya Magetsi – Mphamvu imene dziko la Malawi imafuna imachokera ku zinyalala ndi zachilengedwe choncho kuononga zachilengedwe kumathandizira kuti mpweya oipa wamlengalenga uchulukirechulukire. Izi zimakulirakulira pamene matauni akukula komanso pamene anthu akuchokera kumudzi kukakhaa ku tauni chifukwa kukhala mmalo osavomerezedwa kumadalira zachilengedwe. Njira zimene zaikidwa mundondomeko iyi ndi monga kupititsa patsogolo ukadaulo ndi njira zopezera mphamvu yodzibwezeretsa yokha ndikuchepetsa mtsonkho omwe umaperekedwa ku njira ngati zimenezi, kutenga njira zogwirizana ndi kusintha kwanyengo potukula mphamvu zamagetsi, kupereka njira zapadera zopezera mphamvu zamagetsi kwa amene amagwiritsa ntchito bwino mphamvuyo, kubzala mitengo ndi kulimbikitsa kugwiritsa ntchito zinthu zokhudza mitengo kapena nkhalango,

kulimbikitsa anthu kutsatira lamulo loretsa kupanga makalaa, kulipira kuboma pazinthu zakunkhalango, anthu akumidzi kusamala zachilengedwe, kupanga ma buliketi ndi kulimbikitsa kuumba njerwa posaononga zachilengedwe.

Nkhalango – Nkhalango zomagwira ntchito yosunkga mphweya oyipa wa kaboni ndipo zakhala zikutha chifukwa chakuonongeka kwachilengedwe zimene ndi zotsatira kamba ka anthu kufuna malo olima ndi nkhu. Kusintha kwanyengo kumakhudzanso nkhalango kudzera ku zilala zomwe zimayambitsa moto olusa, ndi kumasinthesintha kwa matenthedwe a mitundu a zachilengedwe komansomitengo. Njira zomwe zakhazikidwa pothana ndi vutoli ndimongakupititsa patsogolo ilimi wa mitengo ndi mbeu, kudzala ndi kusamala mitengo, zilango ndi kulimbikitsa lamulo kwa anthu a bizinezi yamatabwa, lamulo lothetsera moto olusa, kuchepetsa vuto lodalira zachilengedwe ngati nkhu ndikupereka zinthu zapadera zopezera mphamvu ya magetsi, chidziwitso cha udindo wa nkhalango, kupititsa patsogolo umoyo wa anthu amadera akumidzi, kupititsa patsogolo ndondomeko yakafukufuku pa nkhu yosamalira zakutchire ndi zachilengedwe, kupititsa patsogolo zones zankhalango ndikuunika mmene zikuyendera.

Zachilengedwe, zakutchire ndi Zokopa Alendo – Ndondomekoyi ikufuna kuphatikiza kusintha kwanyengo ku zokopa alendo ndi zankhalango kudzera mu njira izi: Kugwiritsantchito ndondomeko yosamalira zakutchire ndi zokopa alendo, kuphatikizapo zinthu zochepetsa kusintha kwanyengo, kupereka chidziwitso pa udindo wa zankhalango pa nyengo, kuunika phindu la anthu ndi zachuma zakasamalidwe ka zachilengedwe zones, kafukufuku wa phindu la zachilengedwe zonsendi ntchito zake.

Ulimi wa Nsomba – Ulimi wansomba udzakhudzidwanso ndi kusintha kwanyengo kudzera ku kuuma kwa mitsinje ndi Nyanja ndi kusinthesintha kwa matenthedwe. Njira zimene zaikidwa mundondomeko imeneyi ndi monga izi kupititsa patsogolo luso la ulimi wa nsomba, kukonza uthenga wabwino, kuteteza madzi ndi kusamala Madera amene amapereka madziwo, kukonzanso ntchito zones zauimi wa nsomba ndi kuchita kafukufuku wa ulimi wa nsomba.

2- Kuthetsa Kusintha kwanyengo

Izi zimatanthauza ntchito iliyonse yofuna kuchepetsa mipweya yoipa ya mlengalenga pofuna kuchepetsa zotsatira za kutentha kwa dziko lonse lapansi. Ndondomekoyi ikufunanso kuchepetsa mipweya yoipayi kudzera mu ntchito zakagwiritsidwe ka malo, ulimi ogwirizana ndi kusintha kwanyengo, chitukuko choyenera, kugulitsa kaboni pochita ntchito zoyenera. Ndondomekoyi ikufotokoza njira izi zothana ndi kusintha kwanyengo:

Mphamvu – Kukonza ndi malonda a zipangizo zamakono zogwiritsa ntchito mafuta a petulo ndi efinolo komanso kupititsa patsogolo luso ndi njira zosunga mphamvu komanso zotulutsa kaboni ochepa.

Makampani – Kupititsa patsogolo makampani amene amagwiritsa ntchito zinthu zosunga kaboni, kumupanganso ndikugwiritsa ntchiyo moyenera, makampani okopa alendo, kulimbikitsa ndikuchita ntchito yandondomeko pa makampani osamala zinyalala, makampani kutngapo mbali pochepetsa mipweya yoipa, mabngwe kuchepetsa zinyalala komanso kuti ikhale mbali yantchito yawo, kuzipanga ndikuzigwiritsanso ntchito.

Kusamalira Zinyalala – Kuyang’anira ndikuunika kwa mipweya yoipa ndi mauthenga ake, kuchepetsa mipweya yoipa yochokera ku magalimoto, kubwezeretsa maenje amene ali ndi zoipa pakuwakwilira, kupititsa patsogolo kuzipanganso zinyalala munjira ina ndikugwiritsa ntchito ndikucheosa zinyalala.

Njira Yachitukuko chabwino – Kupititsa patsogolo ndikukweza njira ndi chitukuko choyenera ndi ntchito zake, kupereka ndalama zochepetsera kaboni, kuika ntchito zachitukuko chabwino mu ndondomeko za Magawo osiyanasiyana ndi kupereka chidziwitso pa ntchito zonse zachitukuko choyenera.

Kusamalira Nkhalango – Pkupititsa patsogolo ndodomeko ndi njira yochepetsera kusintha kwanyengo, kunetsetsa kuti nkhalango zikukhazikitsidwa, kubwezeretsa achilengedwe, kuteteza Madera a amadzi ndi kusamalira nthaka, kulimbikitsa ndondomeko ndi lamaulo lothetsa kuononga nkhalango ndi moto olusa ndi kupititsa patsogolo kudzala mitengo mu ndondomeko zonse zachitukuko.

Ulimi – Kuonjezera masungidwe a kaboni kudzera mu ulimi wa mlera nthaka ndi ulimi wa mbeu ndi mitengo komanso kulumikiza ndondomeko za Magawo onse.

Zantengatenga ndi Mtokoma – Kuchepetsa kwa mipweya yochokera ku magalimoto, Kuyang’anira ndi kuunika mipweya yochokera ku magalimoto, kagwiritsidwe ntchito ka zoyenera za mipweya ya magalimoto ndi kukwaniritsa ndondomekoyogwiritsa ntchito efinolo ndi petulo.

Zanyumba ndi chitukuko cha zomangamanga – Luso ndi nira zabwino zopezera mphamvu pa zomangamanga ndi kupereka kuthekera kwa mabizinezi mu chitukuko.

3- Kupereka Upangiri, Maphunziro ndi Chidziwitso

Cholinga ndi kuonetsetsa kuti pali mauthenga abwino ndipo akuyenda bwino kwa onse ougwiritsa ntchito. Cholinga china ndi kupeeka upangiri pa kusintha kwanyengo mdziko muno ndi kupititsa patsogolo kthejera kwa magulu pogawana mauthenga ndi maphunziro ndi kupereka chidziwitso.

Njira zimene zaikidwa ndi monga kuonjezera kapezedwe ka mauthenga, kuunikira kwa uthenga ndi kusinhasintha kwa zinthu zanyengo ndi zachilengedwe, kulimbikitsa kuyang'anira zanyengo ndi zachilengedwe kudzera ku mabungwe ndi anthu komanso kuthejera kwamabungwewo pa izi, kupezeka kwa mauthenga kuti athandize pa uneneri wa kusintha kwanyengo, maphunziro pa kasamalidwe ka ziopsezo zakusintha kwanyengo ndi maphunziro a magulu okhudzidwa pophatikiza kusintha kwanyengo muntchito zawo. Njira zina ndi monga kupititsa patsogolo chidziwitso kwa opanga ndondomeko, kuikamo nhani zakusintha kwanyengo mu ndondomeko yophunzilira ana asukulu, kukhazikitsa luso pamaphunziro okhudza kusintha wanyengo ndi kupereka chithokozi kwa anthu ali ndi luso pa kusintha kwanyengo, kulimbikitsa udindo wa dziko la Malawi pazokambirana zachithandizo pantchito zakusinha kwnayengo ndi maiko akunja, kuperka upangiri ku mabungwe amaphunziro, azasayansi, mabungwe omwe siaboma, nyumba zofalitsa nkhani ndi maboma ang'onoang'ono.

4- Kupereka chuma pothana ndi kusintha kwanyengo

Ndondomekoyi ikufuna kuonjezera mwayi opeza chuma chothandizira ntchito zothana ndi kusintha kwanyengo kudzera poonjezera ndalama mu ndondomeko yachuma yaboma, kupeza ndalama kuchoka ku mabungwe akunja ndi kutengapo mbali kwa makampani. Zolinga zandalama zakusintha kwanyengo ndi kuonjezera ndalama mu ndodndomeko za chuma, kupeza ndalama ku maiko akunja ndikupereka chithokozi ku makampani.

Njira zambiri zafotokozedwa mundondomekoyi ndipo ndiizi, lamulo lolipiritsa potulutsa zinthu zomwe zibweretse kusintha kwanyengo, kuthandizira mabungwe kupempha thandizo ndi ndalama zothandizira ntchito zakusintha kwnayengo ndi kupereka luso ndi chidziwiso polemba zikalata zopemphera ndalama zantchitoyi ndi kthooza makampani omwe akuchitapo kanthu panthcito zakusintha kwanyengo.

5- Kulumikizitsa Mabungwe

Nthambi ndi maunduna amafuna kuika ntchito zakusintha kwanyengo mu Magawo awo. Kuphatikiza apo pakufunika kulimbikitsa mabungwe ndikuwalumikizitsa kuphatikizapo mabungwe aboma, makampani, anthu onse, ndi makomiti apaboma. Cholinga cha ndondomekoyi ndikulimbikitsa mabungwe mdziko muno ndikuonetsetsa kuti pali kulumikizana kwabwino pa nkani yakusintha kwanyengo. Zolinga zing'onozing'ono zina ndi kulimbikitsa mabungwe ndikupanga kuthekera paboma ndi athu pogwira ntchito zakusintha kwanyengo.

6- Chiwengero cha Anthu

Chiwerengero chikamakwera chimakhudzanso kusintha kwanyengo. Cholinga mkuti tiike ntchito zakusintha kwanyengo mu mchitukuko pofuna kuchepetsa umphawi, kuteteza zachilengedwe ndikuchepetsa kusafanana pazochitika. Zolinga ndi kuika nkhani za chiwerengero cha anthu mu ntchito zakusintha kwanyengo, kupititsa patsogolo kulera ndi kuhetsa kuchulukana kwammadera pokhazikitsa matauni akumidzi ndi kubweretsa ntchito.

Njira zokwanitsira ndi; Kupititsa patsogolo ndondomeko zokhazikika pozochitachita, kupereka mauthenga wakulera, kuganizirapo mmene chiwerengero chikuyendera pa mapulani achitukuko, kukonza zamaphunziro, kukweza chidziwitso pamaphunziro, kukweza za umoyo, kuthandira kupereka mphamvu kwa amayi, kukhazikitsa matauni kumidzi, ntchito zochepetsa kusintha kwanyengo, ntchito zangozi zogwa mwadzidzidzi ziunikenso zaumoyo ndi kupanga kuti magulu onse atengepo mbali pantchito zakusintha kwanyengo.

7- Kafukufuku, kukhazikitsa luso ndikupereka ndikuyang'anira m'mene zikuyendera

Ndondomeko yakusintha kwanyengo imafuna kupititsa patsogolo nthcito zakusintha kwanyengo ndi upangiri ndi upereka ndalama mokwanira. Zolinga ndi kupititsa patsogolo kumvetsetsa kwa kusintha kwanyengo, kuyang'anira zakusintha kwanyengo, ndondomeko zoyenera, kugwiritsa ntchito luso labwino,kafukufuku pothetsa kusintha kwanyengo.

Ndondomeko ikufotokoza njira izi popanga kafukufuku wzosowa ndi zoyenera kuchita, kulimbikitsa ndi kuthandizira kafukufuku wa kusintha kwanyengo,

kupereka luso ndi upangiri, kukonza kayang'aniridwe ka nyengo ndi mabungwe, Kulemba ndi kuvomereza zidziwitso zamakolo, kuyang'anira ndi kuunika ntchito zakusintha kwanyengo, kulumikizana ndi mabunwe ena, kupititsa patsogolo kafukufuku ndikuthandizira njira zokonza kafukufuku wadziko pa nkhani yakusintha kwanyengo.

8- Zinthu zoonjezera ndi Magulu Ovutika

Malamulo

Dziko la Malawi lili ndi ndondomekondi Malamulo okwana 22 okhudzana ndi kusintha kwanyengo, chitukuko chazachuma, ndichilengedwe. Ndongomeko yakusintha kwanyengoidzakhala yaikulu yopezerapo zoyenera kutsatiridwa ndi magulu amene amakhudzidwa ndi kusintha kwanyengo ngati gawolofunika lachitukuko. Idzaperekanso mwayi kundondomeko zina kupanga njira za mapulani aboma. Cholinga chandongomeko ndikuika nkhani zakusinha kwanyengo mundondomekomndi ntchito pokozanso ndi kukonza Malamulo okhudzana ndi kusintha kwanyengo.

Njira zokwaniritsira zolingazi ndi izi: kukonzanso ndondomeko zakale, kuphatikiza ntchito zakusintha kwanyengo m'mapulani am'maboma ndi zofuna zakusintha kwanyengo mu njira zikuluzikulu zachitukuko.

Kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo ndi magulu ovutika

Cholinga chandongomeko ndi kuika nkhani za jenda ndi magulu ovutika mu ntchito zakusintha kwanyengo. Zolinga zenizeni ndimonga kuphatikiza maguu oopsezewa mu ntchito zochepetsa ndi kuthetsa kusintha kwanyengo, kupereka luso ndi upangiri wa mapulani ndi ntchito.

Ndongomeko ikufotokoza njira zosiyanasiyana zokwaniritsira cholinga ndi monga; kuganizira ndi kutengapo mbali kuntchito kwa magulu ovutika muntchito ya kusinha kwanyengo ndikuchita ntchito yandongomeko yakusintha kwanyengo, kuikamo ntchito zamagulu ovutika poyang'anira ndi kuunika ntchito, kupititsa patsogolo luso lomwe chikhalidwe chimalimbikitsa komanso zoti anthu ovutika akhoza kukwanitsa.

Makampani ndi anthu kutengapo mbali


Anthu amakhudzidwa ndi kusintha kwanyengo pamene makampnai amathandizira pokweza chitukuko chadziko ndikusamala zachilenedgedwe choncho kutengapo mbali kwawo mkofunika. Cholinga chandongomeko ndikufuna kupereka mwayi kwa makampani ndi anthu kutengapo mbali pa ntchito zakusintha kwanyengo komanso ntchito zachitukuko. Zolinga

zing'onozing'ono zafotokozedwa mundondomekoyi ndipo ndi kupititsa patsogolo kutengapo mbali kwa aliyense muchitukuko cha kusintha kwanyengo, kupititsa patsogolo kutengapo mbali pantchito zakusintha kwanyengo, kuojezera maubale a magulu pogwira ntchito, kumva maganizo amagulu onse pofuna kuti aliyense atengepo mbali.

Ndondomekoyi ikufotokoza njira izi; kupititsa patsogolo maubale amabungwe pantchito yachitukuko yakusintha kwanyengo, kupereka chithokozo cha malonda pofuna kukweza chitukuko chokhazikika, kupititsa patsogolo makampani kupeza ndalama zakusintha kwanyengo kuti agwilire ntchito ndi kugawana mauthenga kuphatikizaponkhani za zimene zikuyenda bwino kudzera mu misonkhano ya dziko ndi ofalitsa nkhani.

6.0 Magulu Ogwira ntchito ya ndondomeko

Pali magulu ambiri amene akugwira ntchito m'magawo onse amene akuyenera kuchitapo kanthu pa ntchito yakusintha kwanyengo: Magulu akuluakulu ndi monga: boma, mabungwe omwe siaboma, makampani, azamaphunziro, mabungwe othandiza, makomiti achitukuko ku midzi, anthu onse ndi maguu ovutika. Onani zili m'musizi.



7.0 Njira zokwaniritsira ndondomekoyi ndiziti?

Ndondomeko yothana ndikusintha kwanyengo idzakwaniritsidwa potsatira njira izi;

i. Kukhazikitsa Pulani ya dziko

Boma mogwirizana ndi magulu akuluakulu amene afotokozedwa, adzakonza ndikukhazikitsa pulani yadziko pofuna kukwaniritsa ndondomekoyi.

ii. Kuika nkhani zakusintha kwanyengo mu Magawo achitukuko ndi magulu ogwira ntchito.

Magulu akuluakulu aikidwa m'mwambamu adzaunikanso ndikuikamo nkhani zakusintha kwanyengo mu Magawo ofunika, maunduna ndi mapulani a mabungwe ena.

iii. Kuunika m'mene zinthu zikuyendera

Kuunika kawirikawiri kwa ntchito yothana ndikusintha kwanyengo ndikupereka upangiri m'emene ndondomeko ongatsatiridwe ndi magulu onse. Kuphatikiza apo padzakhala kuyang'anira ndi kuunika zotsatira zakusintha kwanyengo ndi ntchito zake.

8.0 Zotsatira za Ndondomeko

Izi ndi zotsatira zisanu ndi ziwiri za ndondomeko yakusintha kwanyengo;

- Kuchepa kwa chiopsezo cha zotsatira zakusintha kwanyengo m'dziko muno
- Mipweya yoipa yamlengalenga kuchepetsedwa ndi kukhala mlingo wake oyenera m'Malawi
- Chidziwitso chokwanira pa zotsatira zakusintha kwanyengo, pochepetsa ndi kuthetsa vutoli
- Kupita patsogolo kokhala odzidalira ndiolimba pankhani yakusintha kwanyengo
- Kulumikizana ndikuvomerezana kwandondomeko zosiyanasiyana
- Kukwera kwa ndalama mundondomeko yazachuma yaboma pantchito yothana ndikusintha kwanyengo
- Kuika zinthu zina zofunika mundondomeko, njira ndi ntchito zogwiridwa.

9.0 Mau Omaliza (Kuphweza Mphongo)

Pomaliza kusintha kwanyengo kukuchitika padziko lonse lapansi, kukukhudza Magawo onse achitukuko. Zotsatira zake, ntchito yochepetsa ndi kuthana

ndikusintha kwanyengo, kupereka luso, ndi kupereka kuthekera kumafuna mgwirizano waukulu pakati anthu mdera, mdziko ndi dziko lonse lapansi. Kuyang'anira kusintha, muchilengedwe ndi umoyo wa anthu, kukhoza kukwaniritsidwa ndi kuunika zizindikiro zikulizikulu ndikumapereka zovuta ndi m'mene zinthu zikuyendera kuti ntchito ichitike.

Kuthokoza ndi Kusamba m'manja

Ndnondomeko mwachiduleyi yapangidwa ndi thandizo andalama kuchokera kubungwe la UKAID kudzera ku bungwe la ActionAid pa ntchito ya kukhala okonzeka pachilichonse. Zimene zalembedwa mumkabukuka ndi zofuna zabungwe la CISON ECC ndipo izi sizikuimira maganizo a UKAID.

Kotenga Mauthenga

Boma la Malawi (2015), Nondomeko yothana ndikusintha kwanyengo, Unduna wa zachilengedwe, Mphavu ndi Migodi, Nthambi yoona zachilengedwe, Lilongwe, Malawi.

Boma la Malawi, (2010), Lipoti la m'mene chilengedwe chilili, Unduna wa chilengedwe, Mphamvu ndi Migodi, Nthambi yoona zachilengedwe, Lilongwe, Malawi.

Mukafuna zambiri Lumikizanani ndi

**The National Coordinator
Civil Society Network on Climate Change (CISON ECC),
P.OBox1036,Lilongwe,Malawi.
Email:cisonecc@cisoneccmw.org
www.cisonecc.org**